STUDENT NAME______________________________________________FORM 4____

# ST MARY'S GIRLS SECONDARY SCHOOL

**2021MALAWI SCHOOL CERTIFICATE OF EDUCATION MOCK EXAMINATION**

# Chichewa

Lachitatu, 11 August Nthawi: 2hrs

**PAPER III** **08:00-10:00**

**(Malikisi 70)**

**Malangizo:**

1. **M'gawo A:** Onetsetsani kuti pepalali lili ndi masamba otsindikizidwa khumi.
2. **M'gawo A :** Yankhani mafunso onse. **(Malikisi 30)**
3. **M'gawo B:** Yankhani mafunso awiri okha. **(Malikisi 40)**
4. **Lembani** nambala yanu ya mayeso pa mwamba pa tsamba lililonse loyankhirapo.
5. M'chitebulo chili pambalipa onetsetsani funso lililonse lomwe mwayankha pochonga mbokosi lomwe lili kutsogolo kwake.
6. Perekani pepalali kwa oyang'anira mayeso nthawi ikakwana

| Funso | Chongani funso ngati mwayankha | Muno musalembemo | |
|---|---|---|---|
| 1 | | | |
| 2 | | | |
| 3 | | | |
| | | | |
| | | | |



FiloKin Edu | The wise learn together. | Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com

**GAWO A (Malikisi 30)**

**Nkhani za Mchezo ndi Zolembedwa**

**Langizo**: Yankhani mafunso onse m'gawo lino

1. Werengani ndakatulo ili mmunsiyi ndipo muyankhe mafunso otsatirawo

**Umodzi wa nyerere**

Ndaima panjira ndicheze
Ndicheze ndi nyerere
Sizipatsa moni
Kutangwanika kokhakokha
Chodabwitsa ndachiona
Umodzi pantchito yawo
Kupuma sizifuna
Ulesi ndi mtsamiro
Mtsamiro wa Satana ati
Phunziro ilo.

Kuyenda kwawo pamodzi
Posamuka kufuna masasa
Ulendo wawo tsogozane
Katundu zitengezana
Zimanga mudzi, zikhazikika
Nkhondo zithandizana
Ntchito sizifunira m'yang'aniri
Katundu akakula zithandizana
Akalemera, zidulirana
Phunzira ilo.

(EJ Chadza)

**Mafunso**

a. Kodi akuyankhula mu ndakatuloyi ndani?

_______________________________________________(malikisi 1)



FiloKin Edu | The wise learn together. | Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com

b. Tchulani mfundo ziwiri m'ndime yoyamba zomwe zikutsimikizira kuti nyerere zimatangwanika kwambiri.

______________________________________________________________

______________________________________________________________

__________________________________________________(malikisi 2)

c. Ndi zinthu ziwiri  ziti zomwe nyerere zimachitira limodzi mosonyeza mgwirizano

______________________________________________________________

______________________________________________________________

__________________________________________________(malikisi 2)

d. Perekani mavuto awiri omwe angadze ngati anthu sachitira zinthu pamodzi ngati nyerere

______________________________________________________________

______________________________________________________________

__________________________________________________(malikisi 2)

e. i. Perekani chitsanzo chimodzi cha mvekero kuchokera mndakatuloyi

___________________________________________________(malikisi 1)

ii. Tchulani mtundu wa ndakatuloyi

___________________________________________________(malikisi 1)

f. Perekani matanthauzo  a mawu otsatirawa

i. Msasa

________________________________________________________

____________________________________________(malikisi 2)

ii. Myang'aniri

________________________________________________________

____________________________________________(malikisi 2)

g. Perekani phunziro limodzi lomwe tingapeze kuchokera pa makhalidwe ndi machitidwe a nyerere.

______________________________________________________________

__________________________________________________(malikisi 2)



FiloKin Edu | The wise learn together. | Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com

2. Werengani nkhani ili m munsiyi ndipo muyankhe mafunso otsatirawo

**Masiku sakoma onse**

Anthu adafika ku msonkhano womwe adayitanitsa Dziwa, m'modzi wa ogwira ntchito pa kampani ina yogulitsa zipangizo za magetsi. Izi zidali chonchi chifukwa anthuwo adali ndi chidwi kuti akamve chomwe chidatsitsa dzaye kuti njovu ithyoke mnyanga. Iye adayamba kuyankhula.

'Akuluakulu ndikufuna kukuthokozani nonse chifukwa chobwera kuti mudzadzimvere nokha, pajatu zakumva kupweteketsa mutu.
Msonkhanowu siwanga wokha ayi koma ndiwatonse. Monga mukudziwa kuti pakampani pano mavuto sakutichoka ayi, takhala tikulandira madandaulo wokhuza katundu amene timapereka kwa makasitomala athu. Ena amabwera kudzatithira mphepo pompano pamene ena amabwera kudzatibwezera kumene kuti zinthu zathu ndi zakabweremawa. Tsono tati tigwirizane kuti tikafunse mabwana athu kumtundako kuti vuto ndi chiyani? Zoona kampani yayikulu ngati ino ingalephere kugula zinthu zolimba? Amenewa adzaona ngati ife ndi ofuka utsi, nkhubzi zimenezi zidziwanso kuti ife si anthu amasewera."

Tiyeni komweko akatiuze basi!' Adatero anthu onse pamodzi. Panthawiyi mtsogoleri uja adachita mantha ndipo adapempha anthu aja kuti akhale kaye chete. Kenaka adapitiriza kuyankhula.

'Akuluakulu, ndikudziwa kuti mu umodzi muli mphamvu koma ndipemphe kuti bwanji tisankhe anthu angapo kuti akatitulire madandaulo athuwa.

Sibwino kuti tonse pano tinyamuke tikafike ku amofesi. Chimenecho n'chipwirikiti. Anthuwo adagwirizana ndi ganizolo ndipo nthumwi zidasankhidwa.

Tsiku litakwana nthumwi zidakumana ndii bwana wamkulu ndikumufotokozera madandaulo awo. Iye adawatsimikizira kuti achitapo kanthu. Nthumwi zija zidatuluka muofesimo zili zosangalala podziwa kuti akuluakulu ndi m'dambo mozimira moto.



FiloKin Edu | The wise learn together. | Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com

Kafukufuku wa kagulidwe ka katundu pa kampanipo adakhazikitsidwa ndipo adayambika. Padali chipwirikiti pa kampanipo pajatu kanthu n'kavumbu kadavumbula mende pachisa. Adayamba ndi kalaliki woyang'anira za chuma, Kathyali, yemwe adati zimenezo koma bwana wake ndiye akuzidziwa bwino iye kwake kudali kulemba zomwe wauzidwa. Ofufuza aja sadalekere pomwepo koma kumpanikiza mkuluyo za momwe katunduyo amagulidwira. Iye adati sakudziwa komwe anthu omwe amawagulitsa katundu amakatenga katunduyo. Ndiye poti kanthu n'khama phwiti adakwatira njiwa, akafukufukuwo adayitanitsa wamalondayo ndikumfunsa. Zidali zomvetsa chisoni kumva kuti iwo adauzidwa kuti azikagula katundu wotsika mtengo koma uko azigulitsa mokwera. Izi zidali zadala kuti ndalama zinazo azigawana bwanayo ndi wamalondayo.

Akafukufuku aja adasangalala poti adadziwa gwero la mavuto apakampani paja ndipo adakafotokozera bwana wamkulu zomwe adapeza. Anthu ena ajanso adasangalala kuti choonadi chidadziwika.

Posakhalitsa anthu onse adakhudzidwa ndi mchitidwewu adafufuzidwa ndi bungwe lowona za katangale ndi ziphuphu. Ena ambiri anamangidwa ndikupatsidwa chilango chokakhala kundende kwa zaka zambiri.

Tsopano yankhani mafunso otsatirawa

a. i. Kodi Dziwe adali ndani munkhaniyi?

_______________________________________________

_______________________________________________(malikisi 1)

ii. Nanga chomwe chidachititsa kuti msonnkhanowu uyitanitsidwe ndi chiyani?

_______________________________________________

_______________________________________________(malikisi 1)

b. N'chifukwa chiyani anthu adapita kumsonkhanowu mwaunyinji?

_______________________________________________

_______________________________________________(malikisi 1)



FiloKin Edu | The wise learn together. | Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com

c. Fotokozani gwero la mavuto omwe adali pa kampanipa.

________________________________________________

_______________________________________(malikisi 2)

d. Perekani zotsatira ziwiri za m'chitidwe womwe ukuchitika m'nkhaniyi

________________________________________________

________________________________________________

________________________________________(malikisi 2)

e. Perekani matanthauzo a zining'a zotsatirazi kuchokera munkhaniyi

i. kudzatithira mphepo

_________________________________________(malikisi 1)

ii. ofuka utsi

_________________________________________(malikisi1)

iii. nkhubzi

_________________________________________(malikisi 1)

f. Pezani mawu munkhaniyi omwe akutanthauza

i. Anthu ogula malonda

_____________________________________(malikisi 1)

ii. Oimira anzawo

_____________________________________(malikisi 1)

g. Lembani mkuluwiko umodzi womwe wagwiritsidwa ntchito munkhaniyi

_________________________________________(malikisi 1)

b. Tsimikizani popereka mfundo imodzi yosonyeza kuti anthu apakampaniyi adali adongosolo

________________________________________________

________________________________________(malikisi 2)



FiloKin Edu | The wise learn together. | Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com

**GAWO B (Malikisi 40)**

**Langizo**: Yankhani mafunso awiri mndime zofotokozedwa bwino

3. **Nthondo (Samuel Josia Nthala)**

   a. Fotokozani mfundo zinayi zoonetsa kuti apangakhani ena anali ogwirizana m'nthano ya Nthondo. (malikisi 20)

   **KAPENA**

   b. Atengambali ena m'buku la Nthondo anali olimba mtima. Fotokozani popereka mfundo zinayi. (malikisi 20)



FiloKin Edu | The wise learn together. | Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com

FiloKin Edu | The wise learn together. | Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com

4. **Chamdothe ndi zisudzo zina (S. Likongwe ndi W. Nkhoma)**

   a. **Zikani (Smith Likongwe)**

      Anthu ena mu sewero la Zikani ankaphwanya ufulu wa maphunziro a ana. Tsimikizani popereka zitsanzo zinayi. (malikisi 20)

**KAPENA**

   b. **Mudzi wa mfumu Tandwe (Wisdom Nkhoma)**

      Fotokozani nkhanza zinayi zomwe atengambali ena achitira anzawo mu seweroli. (malikisi 20)



FiloKin Edu | The wise learn together. | Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com

*Mafunso athera pano*



FiloKin Edu | The wise learn together. | Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com